NAMBALA YA MAYESO .: ____________________________

# THE LILONGWE CITY EXAMINATION BOARD

## 2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATIONS

# CHICHEWA

**(100 Malikisi)**

**Subject Number: P165**

**Nthawi: 2hr 15min**
**1:00 – 3:15pm**

**Tsiku: _____/ ______/ 2024**

**DZINA LA OPHUNZIRA:** ____________________________________________________________
**(*Kuyamba ndi bambo)***
**DZINA LA SUKULU:** ______________________________________________________________

**Malangizo**

1. Pepalaili lili ndi magawo **anayi** Gawo A, B , C ndi D
2. Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
3. Lembani chimangirizo kapena kalata mu gawo A ndipo muyankhe mafunso onse mu gawo B, C ndi D
4. Yankhani mafunso a mu gawo B ndi C m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse
5. Yankhani mafunso a mu gawo D pozungulirza lembo lokhoza pafunso lililonse
6. Muchitebulo chili pamwambachi onetsetsani funso lililonse lomwe mwayankha **pochonga** mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
7. Perekani kwa **oyang'anira mayeso** pepala lonseli nthawi ikakwana

| Mafunso | Chongani funso lomwe mwayankha | Muno musalembemo kanthu | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 – 10 | | | |
| 11 – 15 | | | |
| 16 – 20 | | | |
| 21 – 25 | | | |
| 26 – 30 | | | |
| 31 – 35 | | | |
| 36 – 40 | | | |
| 41 – 45 | | | |
| | | | |

 **Turn over**

## GAWO A (MALIKISI 30)

**Langizo**: Sankhani funso **limodzi** lokha la mafunso **awiri** ali m'munsiwa. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena katala yanu asachepere **100** koma asabzole **150 .**

1. Lembani chimangirizo pamutu uwu " **MADZI OSEFUKIRA M'DERA LATHU."** Mwa zina tsatani izi polemba.

   **Ndime yoyamba**
   - Tchulani dera lakwanu komwe madzi adasefukira.
   - Nanga madziwo adasefukira chaka chanji?
   - Chinachitika ndi chiyani kuti madziwo asefukire?

   **Ndime yachiwiri**
   - Fotokozani mavuto omwe anadza chifukwa cha madzi osefukira.
   - Nanga anthu atawona madziwo anathawira kuti.

   **Ndime yachitatu**
   - Kodi mungawathetse bwanji mavuto akusefukira kwa madzi m'dera la kwanu.
   - Nanga boma lingathetse bwanji mavuto amene amadza kwa anthu chifukwa cha madzi osefukira.

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa wa mkulu wa zaumoyo m'boma lanu yomufotokozera matenda omwe agwa m'dera lanu. Polemba tsatani izi:

   **Ndime yoyamba**
   - Mtundu wa matenda omwe agwa m'dera lanu.
   - Zizindikiro za matendawo.
   - Ndi anthu angati omwe akudwala matendawo ndipo amwalira angati?

   **Ndime yachiwiri**
   - Mwachitapo chiyani kuti matendawo asapitirire kufala.
   - Nkhawa yanu ndi yotani pamatendawo.

   **Ndime yachitatu**
   - Mkulu wa zaumoyo achite chiyani kuti matedawo athe.
   - Chisangalalo chanu chidzakhala chotani matendawo akatha.

________________________________________

________________________________________

________________________________________

________________________________________

________________________________________

________________________________________

________________________________________

________________________________________

## GAWO B (MALIKISI20)
## KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawa

### NAMANYADA ANONG'ONEZA BONDO

Kudali chakum'mawa wa tsiku loweruka pomwe mnyamata wina dzina lake Chikondi ankaperekeza wachikondi wake Namanyada ku malo wokwerera basi ya Nanjati. Pa nthawi imeneyi n'kuti misozi yothamanga ndi yotentha ngati madzi ikutsikira m'masaya mwa mnyamatayo. Kumeneko kudali kulira polingalira kuti wachikondi wakeyu amachoka kupita kokagwira ntchito ku Lilongwe
Basi yomwe adakwera Namanyada isadafike, Chikondi ndi wokondedwa wakeyo adali akucheza. Pamenepa Chikondi adamuuza wokondedwa wakeyo kuti chikondi chake sichidzasintha ngakhale atakumana ndi mikwigwirima yotani. Adamuuzanso kuti ndi bwino kuti njoleyo isunge khosi kuti nkanda woyera idzavale mtsogolo. Adamukumbutsanso kuti kunja kuno kwaopsa choncho mkofunika kusamala. Ngakhale mnyamata adafotokoza zonsezi kudali kungotaya nthawi yake chifukwa kwa njoleyo zinkangotulukira mbali ina yakhutu . Zoona zenizeni zidali zakuti Namanyada sankamukonda Chikondi chifukwa adali mphemvu m'dyera kumthiko, kwakwatuke wachabechabe . Basi itafika, Namanyada adauyatsa wa ku Lilongwe. Iye adafika bwino ndipo sadachedwe kupeza ntchito.

Atayamba ntchito ija mtima wake udaloza kwa njonda ina yomwe idali yokhupuka zedi. Sipadatenge nthawi yayitali Namanyada adamusiya Chikondi uja ndipo adakwatiwa ndi njonda ija ngakhale idali ndi mkazi kale. Makolo a Namanyada adayetsetsa kumuletsa koma poti mwana akalira nyanga ya msatsi m'semere imufotere yekha, patapita nthawi Namanyada adapezeka kuti ali ndi pathupi. Atapita ku sikelo ya amayi adamuyeza ndipo adamupeza kuti ali ndi kachilombo koyambitsa edzi ka HIV. Pamenepa adakumbukira malangizo abwenzi lake Chikondi, koma poti madzi akatayika sawoleka,iye adalira ndi kunong'oneza bondo.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pafunso lililonse**

a. Kodi malo omwe adakwerera basi Namanyada ankatchedwa chiyani?
____________________________________________________________malikisi 1

b. N'chifukwa chiyani misonzi ya Chikondi inkatsika m'masaya?
______________________________________________________________________
____________________________________________________________malikisi 2

c. Kodi Namanyada ankafuna mwamuna otani?
____________________________________________________________malikisi 1

d. Chimene Namanyada adapitira ku Lilongwe chidali chiyani?
____________________________________________________________malikisi 1

e. N'chifukwa chiyani makolo a Namanyada ankamuletsa kukwatiwa ndi njoda ija?
______________________________________________________________________
____________________________________________________________malikisi 2

f. Perekani zining'a kuchokera m'nkhaniyi zomwe matanthauzo ake ndi awa:
   i. Mkazi wokongola ___________________________________________malikisi 1
   ii. Mphawi _________________________________________________1malikisi

g. Perekani matanthauzo a mikuluwiko iyi yomwe ikupezeka mnkhaniyi
   i. Madzi akatayika sawoleka
   ______________________________________________________________
   ____________________________________________________malikisi 2

ii. Isunge khosi mkanda woyera idzavale

_______________________________________________

_______________________________________________malikisi 2

h. Fotokozani chifukwa chimene Namanyada adanong'onezera bondo

_______________________________________________

_______________________________________________malikisi 1

i. Chidapangitsa kuti Namanyada ayezetse chidali chiyani?

_______________________________________________

_______________________________________________malikisi 1

j. Lembani mawu ofanana m'matanthauzo ndi otsatirawa kuchokera m'nkhaniyi

i. Pakati _______________________________________malikisi 1

ii. Yolemera _____________________________________malikisi 1

k. Chifukwa chiyani Namanyada sankamukonda Chikondi

_______________________________________________

_______________________________________________malikisi 1

l. Fotokozani phunziro lomwe lili munkhaniyi

_______________________________________________

_______________________________________________malikisi 2

## GAWO C ( MALIKISI 10)

4. Yankhani mafunso otsatirawa

| | | |
|---|---|---|
| Zingalume | : | Ha! Ha! Ha! Wakhala wabetsa maso sadya kutenga zitatu, imodzi banyira, mwakonda pati |
| Phula mtenga | : | Ife ndiye yalimba mkandirotu. Tiweluka ulele basi |

**Mafunso**

a. (i) Kodi malonjewa angakhle apati?

_______________________________________________malikisi 1

(ii) Kodi mawu oti ' banyira atanthauzanji?

_______________________________________________malikisi 1

(iii) Kodi a Phulamtenga ndi ndani mu nkhaniyi?

_______________________________________________malikisi 1

b. Tchulani njira **ziwiri** zomwe tingafalitsire mauthenga

i. _______________________________________________

ii. _______________________________________________malikisi 2

5. **KUPANGA ZIGANIZO**

**Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:**

a. kholophethe

_______________________________________________malikisi 1

b. lemba

_______________________________________________malikisi 1

c. mothimbwidzika

_______________________________________________malikisi 1

d. mlerakhungwa

______________________________________________________________________malikisi 1

e. tsamira mkono

______________________________________________________________________malikisi 1

## GAWO D (MALIKISI 40)

Zungulizani lembo lokhoza A B C kapena D m'mafunso otsatirawa

**Mafunso 6 mpaka 10: Tchulani mitundu ya mawu ali ndi mzere kunsi kwawo**

6. abambo akhala pa mpando
   - A. mperekezi
   - B. mlowammalo
   - C. Mneni
   - D. Mlumikizi
7. Nkhuku yamawangamawanga yayikira dzira.
   - A. Dzina
   - B. Mneni
   - C. Mfotokozi
   - D. Muonjezi
8. Ganizo lanu ndi losamveka
   - A. Mvekero
   - B. Dzina
   - C. Mlowammalo
   - D. Mfotokozi
9. Hehede! Nsomba zathu zikudya bwino
   - A. Mperekezi
   - B. Mlowammalo
   - C. Mvekero
   - D. Mfuwu
10. Zake zonse zabedwa.
   - A. Mlowammalo
   - B. Mfotokozi
   - C. Dzina
   - D. Mneni

**Mafunso 11 mpaka 15: Sankhani mtundu wa nsinjiro zachiyankhulo zotsatirazi**

11. Kodi kudzala n'kwabwino?
   - A. Nseketso
   - B. Mzimbayitso
   - C.Ntchedzero
   - D. Mkuluwiko
12. Chitsa chagwetsa amfumu
   - A. Chining'a
   - B. Nseketso
   - C. Ntchedzero
   - D. Ndagi
13. Wayabwidwa ndi chitedze
   - A. Mkuluwiko
   - B. Chining'a
   - C. Nseketso
   - D. Ntchedzero
14. Kwa eni kulibe mkuwe mutu wa nkhuku n'chiwalo
   - A. Ndagi
   - B. Nseketso
   - C. Mkuluwiko
   - D. Mzimbayitso
15. Kusololoka khosi ngati kadyansonga
   - A. Mkuluwiko
   - B. Ndagi
   - C. Mzimbayitso
   - D. Chifanifani

**Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani mitundu ya aonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

16. Akuyenda mofulumira kwambiri
   - A. Wamakhalidwe
   - B. Wamchitidwe
   - C. Wamaonekedwe
   - D. Wa nthawi
17. Mayeso timaliza kulemba mawa
   - A. Ovomera
   - B. Wamaonekedwe
   - C. Wamalo
   - D. Wa nthawi
18. Toto sindipitako ine.
   - A. Openeka
   - B. Ovomera
   - C. Okana
   - D. Othokoza
19. Dothili likuoneka mwachikasu
   - A. Wamchitidwe
   - B. Wamakhalidwe
   - C. Wachida
   - D. Wamaonekedwe
20. Agogo adakalamba kwambiri
   - A. Wamuyeso
   - B. Owerenga
   - C. Wamchitidwe
   - D. Wamakhalidwe

**Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani komwe maina otsatirawa apangidwira**

21. Konda ine
   - A. Mneni ndi dzina
   - B. Dzina ndi dzina
   - C. Mneni ndi mlowammalo
   - D. Kuchokera ku mneni
22. Utakafumbi
   - A. Mfotokozi ndi dzina
   - B. Mneni ndi dzina
   - C. Mlowammalo ndi dzina
   - D. Dzina ndi dzina

23. Mlimi
    A. Kuchokera ku mneni
    B. Kuchokera ku dzina
    C. Kuchokera ku mlowammalo
    D. Kuchokera ku dzina ndi dzina
24. Ubwino
    A. Pophatikiza mphatikirambuyo ku dzina
    B. Pophatikiza mphatikirammbuyo ku mlowammalo
    C. Pophatikiza mphatikira mmbuyo ku muonjezi
    D. Pophatikiza mphatikirammbuyo ku mfotokozi
25. Ukulu
    A. Pophatikiza mphatikirammbuyo kutsinde la mfotokozi
    B. Pophatikiza mphatikirammbuyo kutsinde la muonjezi
    C. Pophatikiza mphatikirammbuyo kutsinde la mneni
    D. Pophatikiza mphatikirammbuyo ku dzina

**Mafunso 26 mpaka 29: Sankhani mtundu wa msintho wa aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

26. Iye <u>wasambwadzidwa</u> ndi makolo ake
    A. Msintho wochitidwa
    B. Msintho wonyazitsa
    C. Msintho wotsutsa
    D. Msintho wochitirana
27. Amayi <u>amenyana</u> kwambiri kumsika
    A. Msintho wochitsa
    B. Msintho wochititsitsa
    C. Msintho wobwerezabwereza
    D. Msintho wochitirana
28. Nasibeko <u>wamanga</u> mtolo
    A. Wochitira
    B. Wochitirana
    C. Wonyazitsa
    D. Wotsutsa
29. Mkazi wokwatiwa <u>sapitapita</u> kwawo
    A. Wotsutsa
    B. Wobwerezabwereza
    C. Wochitidwa
    D. Wochitirana

**Mafunso 30 mpaka 32: Sankhani ntchito za aperekezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

30. Ana apita <u>ku</u> sukulu
    A. Kusonyeza malo
    B. Kusonyeza mbali
    C. Kusonyeza nthawi
    D. Kusonyeza chipangizo
31. Joni wadya phala <u>la</u> mwana
    A. Kusonyeza mbali
    B. Kusonyeza umwini
    C. Kusonyeza malo
    D. Kusonyeza chipangizo
32. Dzuwa limatulukira <u>ku</u> m'mawa
    A. Kusonyeza umwini
    B. Kusonyeza nthawi
    C. Kusonyeza chipangizo
    D. Kusonyeza mbali

**Mafunso 33 mpaka 35: Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro za mkalembedwe zoyenera**

33.
    A. Mayo! Nditsala ndi yani?
    B. Mayo! nditsala ndi yani?
    C. Mayo nditsala ndi yani.
    D. Mayo nditsala! ndi yani?
34.
    A. ASato adati, mitengo ndi yofunika.
    B. Asato adati, " Mitengo ndi yofunika.
    C. A Sato adati, " Mitengo ndi Yofunika."
    D. A Sato adati, " Mitengo ndi yofunika,"
35.
    A. Ophunzira ali m'kalasi.
    B. Ophunzira ali m'kalasi,
    C. Ophunzira ali m'kalasi?
    D. Ophunzira ali m'kalasi!

**Mafunso 36 mpaka 38: Sankhani mawu oyenera kutsirizitsa mikuluwiko yotsatirayi**

36. Mphutsi zidanenepera ____ kwa alendo.
    A. Kunyumba C. Kubwera
    B. Kumbuyo D. Kuchoka
37. Kutola khobwe ndi ____
    A. Masana C. Mmawa
    B. Madzulo D. Usiku

38. Ukakwera pamsana pa njovu usamati____
    A. Ndiwe bwana
    B. Kulibe mavuto
    C. Ndiwe ochenjera
    D. Kulibe mame

**Mafunso 39 mpaka 41: Sankhani matanthauzo a mawu omse atsekedwa mzere kunsi kwake mziganizo zotsatirazi**

39. Mavuto ndi wambewewe
    A. Wachibwibwi
    B. Wamakani
    C. Waukali
    D. Wachidodo
40. Madzi akumwa amulowa kummero
    A. Kumtima
    B. Kukhosi
    C. Kukamwa
    D. Kummlomo
41. Iye adachita mphumi
    A. Chidodo
    B. Manjenje
    C. Mwayi
    D. Tsoka

**Mafunso 42 mpaka 45: Sankhani mitundu ya nthambi zaziganizo zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwake mziganizo zotsatirazi**

42. Ndibodza kuti Joni wabwera
    A. Nthambi yosaima payokha ya dzina
    B. Nthambi yosaima payokha ya muonjezi
    C. Nthambi yosaima payokha ya mfotokozi
    D. Nthambi yoima payokha
43. Zakuti adyera nyama, sizachilendo
    A. Nthambi yosaima payokha ya dzina
    B. Nthambi yoima payokha
    C. Nthambi yosaima payokhaya muonjezi
    D. Nthambi yosaima payokha ya mfotokozi
44. Iye akuyenda ngati watopa.
    A. Nthambi yoima payokha
    B. Nthambi yosaima payokha ya muonjezi
    C. Nthambi yosaima payokha ya mfotokozi
    D. Nthambi yoima payokha
45. Ana akusewera apowo ndi akwathu
    A. Yoima payokha
    B. Nthambi yosaima payokha ya mfotokozi
    C. Nthambi yosaima payokha ya muonjezi
    D. Nthambi yosaima payokha ya dzina

**MAFUNSO ATHERA PANO**

**NB: Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba asanu ndi atatu**